

Liwu lakuti **kuyambuka** limatanthauza dongosolo losintha kapena kusandulika kuchokela ku makhalidwe kapena machitachita ena kupita ku ena.

**N**dondomeko za zipangizo zaulimi zotsika mtengo (FISPs) ziyenela kupita kumalecheleche ndi kubwezeletsedwa ndi ndondomeko zimene zidzakomele malimidwe osamala chilengedwe, kuyika ndalama mu ntchito zaulangizi zimene zimathandizira malimidwe osamala chilengedwe, kafukufuku ndi chitukuko zokhudza ndi zopangidwa ndi alimi, kuthandiza ndi kuzindikila ndondomeko za mbeu zoyendetsedwa ndi alimi, ndi zomangamanga (madzi ndi miseu) – zones zimene pamodzi, zimapeleka ubwino wobwela patapita nthawi yayitali.



## Kulimbikitsa ndondomeko zimene zimalola aliyense kutenga nawo mbali

- ▶ Alimi komanso alangiza aboma amafunika chithandizo kudzela m'maphunziro a ma luso a malimidwe wosamala chilengedwe.
- ▶ Pali kufunika kwa ma ubale ochoka ku nthabi za maphunziro zosiyanasiyana zimene zimafalikila m'madela a chikhalidwe cha anthu, amabungwe komanso ma luso.
- ▶ Pakuyenela kukhala njira zosiyanasiyana zogawilana nzeru pakati pa alimi, akatswiri a za sayansi, opanga ndi kuyendetsa ndondomeko za boma, pamene gawo lililonse lizidziwitsa linzake zimene likuchita.

## Kutenganso ulamuliro

Alimi ang'onoang'ono ayenela:

- ▶ kukakamiza kuti ayikidwe nawo komanso atenganawo mbali mwa machawi mu ndondomeko za zinthu zimene zimawakhudza;
- ▶ kulondoloza ndi kuchita kaundula wa zotsatila; komanso
- ▶ Kubwela pamodzi motsutsana ndi kuzembetsa kwa chuma ndi zipangizo kupita kwa anthu olemela.

# Kuyambuka kutuluka mu FISP

